PHUNZIRO LA 8

1. Kodi Mulungu analilenga dziko la pasi kuti likhale la angelo kapena Satana ndi ziwanda zake?
-Iyayi.

2. Kodi Mulungu anaŵalengela ndani dziko la pasi?
-Anthu.

3. Kodi pa zinthu zonse zimene Mulungu analenga, chofunika kwambiri ndi chiyani?
-Anthu.

4. Chifukwa chakuti anthu ndi amene anali ofunika kwambiri pa zinthu zonse zimene Mulungu anazilenga, Kodi Iye anaganiza zoŵalenga bwanji anthu?
-Mulungu anaganiza zoŵalenga anthu mu chifaniziro Chake.

5. Kodi Mulungu anaŵalenga bwanji anthu mosiyana ndi nyama?
-Mulungu anaŵalenga anthu mu chifaniziro Chake.

6. Kodi mawu akuti “mchifaniziro Chake” akutanthawuza chiyani?
-Mulungu anaŵapatsa anthu nzeru kuti adzimudziwa Iye.
-Mulungu anaŵapatsa anthu nzeru za mphamvu kuti adzimukonda Iye.
-Mulungu anawapatsa anthu chifuniro kuti adzimusamkha Iye.

7. Kodi pachiyambi, Mulungu anaŵalenga anthu angati?
-Wam’muna m’modzi ndi wamkazi m’modzi.

8. Kodi dzina la mamuna woyamba linali ndani?
-Adamu.

9. Kodi Mulungu anamulenga Adamu kuti akhale oyang’anira chiyani?

-Dziko lonse la pasi.

10. Kodi chifukwa chiyani angelo sayang'anira dziko la pasi?
-Chifukwa chakuti Mulungu analenga anthu kuti adziyang'anira dziko la pasi.

11. Kodi chifukwa chiyani angelo sayang'anira dziko la pasi?
-Chifukwa chakuti Mulungu analenga anthu kuti adziyang'anira dziko la pasi.

12. Kodi pachiyambi dziko la pasi linali lotani?
-Kunalibe minga.
-Kunalibe mtchire.
-Kunalibe zoyipa.

-Zinthu zonse zinali zabwino kwambiri.

13. Kodi amene analipo ndi ndani pamene Mulungu amkalenga dziko la pasi?
-Angelo a Mulungu, Satana ndi ziwanda zake.

14. Kodi Satana ndi ziwanda zake anali osangalala pamene Mulungu analenga dziko labwino kwambiri?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anamaliza kulenga kumwamba ndi dziko la pasi?
-Inde.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:1

1-Chomcho kumwamba ndi dziko la pasi ndi zinthu zonse zokhala m'menemo anamaliza kuzilenga.

-Mulungu anamaliza kulenga zinthu zonse.
-Mulungu anamaliza kuyigwira tchito yonse yimene anayiganizira kuti ayigwire.

-Nthaŵi zina anthu amayiyamba kuyigwira ntchito, koma osayimaliza.
-Nthaŵi zina amuna amayamba kumanga nyumba, koma osayimaliza.
-Nthaŵi zina akazi amayamba kuwumba mbiya, koma osayimaliza.

-Nthaŵi zina anthu amalephera kuyimaliza nthito chifukwa chakuti tchitoyo yimakhala yovuta.

-Nthaŵi zina anthu amalephera kuyimaliza ntchito chifukwa chakuti munthu wina waletsa tchitoyo.

-Koma Mulungu sali ngati anthu.
-Mulungu akayiyamba tchito, amayimaliza.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amati akayiyamba ntchito, samayilephera?
-Chifukwa chakuti Mulungu samasintha.
-Chifukwa chakuti palibe chinthu china chili chose chimene chingamuletse Mulungu kumaliza nthito yake.

-Mulungu akayiyamba ntchito, Iye samayisiya chifukwa chakuti ntchitoyo ndi yovuta

-Mulungu akayiyamba tchito, Iye samayisiya chifukwa chakuti munthu wina wamuletsa.

-Mulungu akayiyamba ntchito Yake, anthu sangathe kumuletsa Iye.

-Mulungu akayiyamba ntchito Yake, Satana ndi ziwanda zake sangathe kumuletsa Iye.

-Mulungu akalonjeza kuti apanga chinthu china chake, nthaŵi zonse amachipanga.

-Tiyeni tiŵerenge chimene anachita Mulungu atatha kulenga kumwamba ndi dziko la pasi.

Tuyeni tuŵerenge Genesesi 2:2-3

2-Pa tsiku lachisano ndi chimodzi, Mulungu anamaliza ntchito yonse yimene anayiganizira kuti ayigwire, ndipo anapuma pa tsiku lachisano ndi aŵiri.

3-Mulungu analidalitsa tsiku lachisano ndi aŵiri ndikuliyeretsa, chifukwa chakuti Iye anapuma pa tsiku limeneli atatha kulenga zinthu zonse.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapuma pa tsiku lachisanu ndi aŵiri?
-Kodi Mulungu anatopa?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanatope atatha kulenga zinthu zonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu samatopa.
-Chifukwa chakuti mphamvu za Mulungu sizitha.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anapuma pa tsiku lachisano ndi aŵiri?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamaliza kulenga zinthu zonse zimene anaganiza kuti azilenge.

-Kodi Mulungu analenga zinthu zonse pa masiku angati?
-Pa masiku asano ndi limodzi okha.

-Kodi kumanga nyumba kumatenga masiku angati?
-Mwina mwake kuposa miyezi yitatu.

-Tawonani zimene Mulungu anazilenga pa masiku asano ndi limodzi okha!

-Mulungu yekha ndi amene anakatha kulenga kumwamba ndi dziko la pasi pa masiku asano ndi limodzi okha.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:4b ndi 6

4-Pamene Mulungu analenga dziko la pasi ndi kumwamba,
6-madzi amkatuluka pasi pa dziko lose la pasi ndikumatsilira pa nthaka.

-Pachiyambi pamene Mulungu analenga dziko la pasi kunalibe mvura.

-Ngati kunalibe mvura, kodi nanga Mulungu amkatsilira bwanji dziko la pasi?

-Pachiyambi, pamene Mulungu analenga zinthu zonse, Iye amkatsilira dziko la pasi ndi madzi aturuka pa nthaka.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:8

8-Tsopano Ambuye Mulungu anatsekula munda chakuvuma kwa Edeni; ndipo munthu amene anamuwumbayo anamukhazika m'menemo.

-Pachiyambi, Mulungu anatsekula munda wokongola kwambiri.
-Mundawo umkatchedwa kuti munda wa Edeni.

-Kodi Mulungu anamutsekulira ndani munda wa Edeni?
-Adamu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutsekulira Adamu munda?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamukonda kwambiri Adamu.

-Pamene Mulungu anatsekula munda, Iye anamuyika Adamu

m’mundamo.

-Kodi Mulungu anamufunsa Adamu kuti akamuyike iye m’munda wa Edeniwo?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanamufunse Adamu kuti akamuyike iye m’munda wa Edeni?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu, Adamu ndi wa Mulungu.

-Apa pali chitsanzo.

-Kodi mamuna akamanga nyumba, nyumbayo yimakhala ya ndani?
-Mamunayo.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mamunayo ndi amene wamanga nyumbayo.

-Kodi mkazi akawumba mbiya, mbiyayo yimakhala ya ndani?
-Mkaziyo.

-Chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mkaziyo ndi amene wawumba mbiyayo.

-Chifukwa chakuti Mulungu anamulenga Adamu, Adamuyo ndi wa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu analenga anthu onse, anthu onse ndi a Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu analenga zinthu zonse, zinthu zonse ndi za Mulungu.

-Pakati pa munda wa Edeni, Mulungu anadzala mitengo yiŵiri yosiyana ndi mitengo yina yonse.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:9b

9-Pakati pa mundawo panali Mtengo Wopereka Moyo ndi Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

-Mtengo woyamba umene Mulungu anadzala pakati pa munda wa Edeni uja unali Mtengo Wopereka Moyo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anadzala Mtengo Wopereka Moyo pakati pa Munda wa Edeni?

-Mulungu amkafuna kuti Adamu adye kuchokera mu Mtengowo ndipoakhale ndi moyo mpaka kalekale.

-Mulungu sanamukakamize Adamu kuti adye kuchokera mu Mtengo Wopereka Moyowo.
-Mulungu amkafuna kuti Adamu asankhe.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu asankhe kudya kuchokera mu Mtengo Wopereka Moyo.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu asankhe moyo.

-Mtengo wachiŵiri umene Mulungu anadzala pakati pa munda wa Edeni uja unali Mtengo Wadziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

-Mulungu anamupatsa Adamu lamulo pa Mtengo Wodziŵitsa zabwino ndi yoyipa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:16-17a

16-Ndipo Mulungu anamulamula munthu uja kuti, “Udzidya zipatso za mu mtengo wina uliwose wa m’mundamu,
17-koma usadye kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.”

-Mulungu anamuwuza Adamu kuti akhoza kumadya ku-
chokera mu mtengo wina uliwose wa m'mundamo, koma
mtengo umodzi asadye.

-Mulungu anamulamula Adamu kuti asadye kuchokera mu
Mtengo Wodziŵitsa zabwino ndi Zoyipa.

-Mulungu amazidziŵa zinthu zimene zili zabwino ndi zimene
zili zoyipa.

-Mulungu amadziwa kuti zabwino ndi zabwino ndipo zoyipa
ndi zoyipa .

-Pachiyambi, Adamu amkadziwa zinthu zabwino zokhazokha.
-Pachiyambi, Adamu samkazidziwa zinthu zoyipa.

-Tiyeni tiŵerenge zimene analankhula Mulungu kuti Adamu
zidzamuwonekera akadzadya kuchokera mu Mtengo
Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:17b

17-[Ndipo Mulungu anati kwa adamu]Usadzadye zi-
patso za mu Mtengo umenewo. Ukadzadya ndithu, udzafa."

-Kodi Adamu akanadya kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa
zinthu Zabwino ndi Zoyipa uja, chinakamuchitikira chiyani?
-Adamu akanafa.

-Kodi imfa ndi chiyani?

-Anthu ambiri amalankhula kuti pali imfa ya mtundu umodzi.
-Mulungu akulankhula kuti pali imfa ya mitundu yitatu.

-Imfa yoyamba, ndi kusiyana ndi Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani kusiyana ndi Mulungu yili Imfa?
-Chifukwa chakuti Mulungu Yekha ndi amene amapereka moyo.
-Chifukwa chakuti moyo onse umachokera kwa Mulungu.

-Lusifala analakwa, ndipo anasiyana ndi Mulungu.
-Adamu anakakhala kuti sanamumvere Mulungu, anakasiyana ndi Mulungu.

-Imfa yachiŵiri, ndi kusiyana kwa moyo ndi thupi.

-Iyi ndi imfa imene anthu ambiri amayidziwa.
-Adamu anakakhala kuti sanamumvere Mulungu, thupi lake linakafa.

-Imfa ya chitatu, ndi kusiyana ndi Mulungu mpaka kalekale Mnyanja Ya Moto Wosatha.
-Adamu anakakhala kuti sanamumvere Mulungu, moyo wa Adamu unakapita ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Adamu anakakhala kuti sanamumvere Mulungu, anakasiyana ndi Mulungu, thupi lake linakafa, ndipo moyo wake unakapita ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Adamu kuti asadye kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi wa Mulungu.

-Mamuna akapanga khasu, kodi khasulo limakhala la mamuna amene walipangayo?
-Inde.

-Mkazi akawumba mbiya, kodi mbiyayo yimakhala ya mkazi amene wawumbayo?

-Inde.

-Mwana akapanga chidole, kodi chidolecho chimakhala cha mwana amene wachipangayo?
-Inde.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu, Adamu ndi wa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu, Mulungu ndi amene anakatha kumulamula Adamuyo.

-Kodi kunali kwabwino kwa Mulungu kumulamula Adamu?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani kunali kwabwino kwa Mulungu kumula-mula Adamu?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anali ndi mzeru zambiri kuposa Adamu.

-Kodi mzibambo amakhala ndi mzeru zambiri kuposa mnya-mata?
-Inde.

-Kodi mzimayi amakhala ndi mzeru zambiri kuposa mtsikana?
-Inde.

-Kodi ndikofunika kwambiri kuti mnyamata adzimumvera mzibambo?
-Inde.

-Kodi ndikofunika kwambiri kuti mtsikana adzimumvera mzi-mayi?
-Inde.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anali ndi mzeru zambiri kuposa Adamu, kunali kofunika kwabiri kuti Adamu adzi-mumvera Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amafuna kuti Adamu adzimumvera Iye?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anali ndi mzeru zambiri kuposa Adamu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkazidziwa zinthu zonse zimene zinali zabwino kwa Adamu.

-Chifukwa chakuti Mulungu amkazidziwa zinthu zonse zimene zinali zoyipa kwa Adamu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kumutchinjiriza Adamu.
-Azibambo amazidziwa zinthu zimene zili zabwino kapena zoyipa kwa anyamata.

-Azimayi amazidziwa zinthu zimene zili zabwino kapena zoyipa kwa atsikana.

-Kodi amene amkazidziwa zinthu zonse zimenne zinali zabwino kapena zoyipa kwa Adamu anali ndani?
-Mulungu.

-Kodi amene amazidziwa zinthu zonse zabwino kwa anthu onse ndi ndani?
-Mulungu.

-Mulungu amazidziwa zinthu zonse.
-Mulungu amkafuna kuti Adamu adzimumvera Iye.
-Mulungu amafuna kuti anthu onse adzimumvera Iye.

-Zowona zenizeni za Mulungu zili mu Bayibulo.

-Mulungu akufuna kuti anthu onse adzimvera zonse zimene Iye analemba Mbayibulo.